

Mulandu

1 M'bukhu la Marko Mutu 16, kuyambira ndime ya 9, ndikufuna kuwerenga. Ndime yopambana, ya za chiukitsiro.

Ndipo pamene iye adauka mamawa tsiku loyamba la sabata, anayamba kuonekera kwa Mariya wa Magadala, amene iye anamutulutsira ziwanda zisanu ndi ziwiri.

Iyeyu anapita kukawauza iwo amene adafokhala naye, ali ndi chisoni ndi kulira misozi.

Ndipo Iwowo, pamene anamva kuti ali ndi moyo, ndi kuti adapenyeka kwa Iye, sanamvera.

Ndipo Zitatha izi anaonekanso Iye m'maonekedwe

ena kwa awiri a iwo ali alikuyenda kupita kumiraga.

Ndipo Iwowa anachoka namauza otsala; koma iwo omwe sanawabvomereza.

Ndipo chitatha icho anaonekera kwa khumi ndi mmodzi iwo okha, alikuseama pachakudya; ndipo anawadzudzula chifukwa cha kusabvomereza kwawo ndi kuuma mtima, popeza sanabvomereza iwo amene adamuona, atauka Iye.

Ndipo ananena nawo, mukani kudziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse.

Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupirira adzalangidwa.

Ndipo zizindikiro izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzatulutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atso pano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka, adzaika manja awo pa odwala, ndipo adzachira.

Pamenepo Ambuye Yesu, atatha kulankhula nawo, analandiridwa kumwamba, nakhala pa dzanja lamaja la Mulungu.

Ambuye anachita nawo pamodzi, natsimikiza mawu ndi zizindikiro zakutsatapo. Amen.

2 Tipemphere. Ambuye Yesu, Tikunena tsopano pamene tikuyandikira mpando wa Atate. Ndipo m'dzina Lanu, Tikhulupirira awa kuti ndi Mawu anu. Tikukhulupirira kuti ndi Mawu otsiriza amene anachokera pamilomo yanu musanakwere kumwamba. Ndipo tikufunsani kuti muwadalitse m'mitima mwathu masana ano, chifukwa cha iwo amene akudwala Tikuthokozani poitana chinantindi kumpando wanu usiku wathawu, ndipo taona mizere yopambana ya amuna, akazi, atate, ana, amai, akubwera motsogozana kudza ku chipinda chopemphereramo. Tikuthokozani chifukwa cha zimenezo Atate. Tsopano tikupemphera kuti muwapatse chuma cha mu ufumu wanu, ndipo pakhale chikhulupiriro pakati pathu masana ano chopangitsa Mawu a Mulungu kukhala owona kwa ife. Ndipo ndi inu nokha amene mungachite izi, Atate, choncho tipempha m'dzina la Yesu Khristu. Amen. (mukhoza kukhala)

3 Tsopano pa phunzitsa langa mazulo ano limene ndikufuna kutenga, likumveka ngati la chilendo. Ndikufuna kutenga limeneli chifukwa cha dzulo, pa chakudya chammawa ndinakumana ndi m'modzi wa anthu okoma zedi, ndipo wakhala kumbuyo kwanga tsopano, woyimira mirandu. Ndipo timakamba za Mulandu, ndipo kwambiri kapena pang'ono unali mulandu wa chipongwe kapena chinachake, umene anawazenga Ambuye wathu. Ndipo ine Ndikukhulupirira kwathunthu kuti munthu ameneyo akanakhala woyenera kuimapano ndikufanizira ndi mabwalo amilandu ya dzikoli chifukwa ndinalankhula za iye kuyambira pamene ndinakumana naye, ndipo Iye... Anthu amandiuza kuti ndiwoyimira milandu wodabwitsa, ndiye ndikudziwa kuti akanamuzenga mulandu woyenera. Ndipo pokhala kuti Yesu sanapatsidwe chiweruzo choyenera...Ndipo iye ndi Mawu. Tonse tikuvomereza izi. Iye ndi Mawu. Tsono Ndawerenga Mawu Ake, ndipo tiwaika Mawuwa pa mulandu masana ano.

Mawu ali pa Mulandu.

4 Nkhani yake nayi, Malonjezo a Mulungu kutsutsana ndi dziko lapansi. Tsono choyambitsa mulanduwa, ndi,

kuswa lonjezo. Ndipo...Ndikuganiza wofunsa mulandu nthawi zonse amaimira chiweruzo. Ndiganiza ndizoon. Ndipo...Satana ndi woimira wosuma, iye akuimira dziko lapansi pa mulandu uwu. Wotsutsana naye ndiye Mulungu. Ndipo mboni Yake ndi Mzimu Woyera. Tsono ndikufuna kuti mpingo, anthu opemphera, akhale nduna zothandiza kuweruza mulanduwo komanso woweruza mulandu kumene. Tiyeni timve za mulanduwo, pamene tikukankha makatani kuti tiwone pamene takhala.

5 Tsopano, musaiwale kuti...chimene tikuwona apa ndi chimene chayambitsa mulandu, ndi Mawu a Mulungu kutsutsana ndi dziko lapansi. Choyambitsa mulanduwo, ndi kuswa lonjezo, kapena titi kuti dziko lapansi likunena kuti Mulungu anapereka lonjezo limene siliri loona. Kumeneko ndiko kuswa lonjezo. "Iye samasunga lonjezo Lake." Ndipo wosuma mulandu pamenepa ndi Satana, amene akuimira dziko lapansi. Ndi wotsutsana naye ndiye Mulungu Mwini. Ndipo mboni yake ndi Mzimu Woyera.

Tsopano tikuuza bwalo kuti likhale chete.

6 Tsopano wosuma mulandu aitana mboni yake yoyamba kuti ayime namulumbirira. Tsopano, ali ndi mboni zitatu masana ano ndikufuna kuzigwiritsa nthito, kani titi omwe akufuna kuwagwiritsa nthito pa mulandu wake. Ndipo mboni zimenezi ndi Bambo Kusakhulupirira, wina ndi Bambo Kukaikitsa ndipo winayo atchedwa Bambo Kusapilira. Tsono izi ndi mboni zotsutsa zimene zikunena kuti, "Mulungu sasunga Mawu Ake. Mawu Ake siowona."

7 Ndiye tikhoza kuona, tisanayambe mulandu kuti-kuti ambiri a m'dziko lapansi amayesa kunena kuti Mawu a Mulungu siowona. Mwachitsanzo, ndangowerenga, ndimawerenga ndemanga za Scofield. Ndiye ndimaganiza za nkhani imene ndinauzidwa. Ndiganiza...Sindikuganiza kuti ndidazinenapo maka maka mu msonkhano uno. Koma mzimayi wina nthawi ina anali ndi kamnyamata kabwino, adafuna adzakhale wolalikira. Koma anali mayi wosauka, adafuna mwana wake aphunzire bwino (chimene mayi aliyense angafunire mwana wake, ngati atayitanidwa motero), Kum'phunzitsa maphunziro apamwamba amene angapezeke chifukwa mayiyo adafuna kuti atero. Kotero anamutumiza ku seminale yopambana imene anaidziwa kuti

angamutumizeko.

8 Chabwino m'nyamatayo anakhala kumeneko pafupi chaka, ndipo tsiku lina mayi wake anadwala koopsyas analinso mwa moyo. Ndipo - anthu anatumizira uthenga ndi matelegalamu. Mayiyu ankakhala yekha. Kuti mwina mwana wake akanabwera chifukwa anadwala ndithu kwambiri, ndiye zinangosakanizana ndi chibayo ndiponso analinso ndi matenda...mumapapo ake, anali pafupi kufabasi. Mtima wake unawonetsa osatinso zabwino. Koterodotolo anayesetsa kuchita zimene amadziwa kuti apulumutse moyo wake, koma matenda anapitirirabe. Koterodotolo anatumiza telegalumu kwa mwana wakeyo ndi kuti, "Pakali pano ukonze za ulendo wa pa ndege, kuti ubwere, chifukwa amayi ako atsala pang'ono kufa." Tsonomnyamatayo, atazunguzika anayamba kukonza zobvalazake, kukonzekera kuti akakwere ndege. Ndipo - ndiye inabwera telegalamu ina tsopano yochokera kwa amayi akewo. "Usabwere mwana wanga. Ine ndachiritsidwa."

9 Ndiye patapita chaka, kapena miyezi isanu ndi umodzi, ndikukhulupirira zinali choncho, mnyamata ujanapita kumudzi, choncho, mnyamata ujanapita kumudzi, Atapatsana moni ndi mayi ake, ndi kumacheza Iye anati, "Amayi pali funso limodzi limene lakhala likundivutabem'malingaliro anga." Nati, "Pamene munadwala kwambiri" nati, "simunandiuze zonse mwatsatane - tsatane, munangondiuza kuti basi ndachiritsidwa, koma simunandiuze zonse mwatsatane - tsatane za m'mene munachiritsidwira."

10 Mayiyo anati, "Mwana wanga, ukudziwa pamunsi apo, pamene panali golosale kale paja?"

"Inde."

11 Pali gulu la anthu amene amapemphera mu chinyumba chimenecho.

"Inde," nati, "Ndikukumbukira za iwo, ndi anthu a Pentekoste."

12 Anati, "Inde ndi choncho." Nati, "Pamene ndinadwala kwambiri," anati, 'kunali mlongo wina wabwino

anabwera kwa ine, ndipo anati, mlongo ife tabwera kuno kudzapemphera pakuti tinamva kuti mumadwala kwambiri ndi kuti mwana wanu ali ku - ku seminare, kuti adzakhale wolalikira. Ndipo pamene tinkapemphera, Ambuye anavumbulutsa kwa ife kuti tibwere tidzapemphere nanu.' Ine ndinati 'chabwino', Iye anati, "Zimenezo zikhala zabwino." Nati, 'Mungadandaule ngati abusa athu atabwera kudzapemphera?' Ndinati, 'Palibe chifukwa chakuti ndikane mlongo. Ndikondwera, ndinatero'. Koterokanabweretsa...Dotolo anati sindidzakhala bwino. Choncho mbusa anabwera nawerenga pa Marko 16. Ndipo anati, "Ichi ndi chimene Baibulo likunena." Ndiye anasanjika manja ake pa mzimayiyo napemphera natuluka ndipo akuti iye. "anachiritsedwa," anatero.

"O"! mnyamata anati, "Amayi!"

Mayi nati, "Kodi sizodabwitsa zimenezo? Mwana wanga? Tangoganizira!"

13 "O," anati, "Amayi zimenezo sizikukhuzana ndi kuchiritsidwa kwanu." Nati, "Mwina mankhwala ena amene anakupatsani Dotolo anali atangogwira ntchito nthawi imeneyo."

14 Mayiyo anati, "O! Iai mwanawanga Adotolo anali atasiya kundipatsa mankhwala kwa masiku awiri, nkumanena kuti panalibe chirichonse chimene akanachita. Anangondiika pa mphweya, ndikumati palibe chimene akanachita. Ndipo ine ndinadwalira dwalirabe."

15 "O," Mnyamamtayo anati, "Amayi, sizinali choncho." Nati, "Mukudziwa kuti amenewo ndi anthu osaphunzira." Nati, "Iwo sakumvetsa. Amangowerenga Baibulo." Nati "Mukuona?" Maiyo anati, "Chabwino, kodi sitiyyenera ife kukhulupirira Baibulo, mwanawanga?"

16 Mnyamatayo anati, "O, zoonu." Nati, "Mayi tiyyenera kulikhulupirira, koma," nati "mukudziwa ku sukulu," nati, "tinaphunzira kuti apo pamene anawerenga pa Marko 16, kuyambira ndime 9 ndi mavesi osatirawo ndi mau osauziridwa."

"Chabwino," Mayiyo anati, "Ulemerero kwa

Mulungu."

17 Mnyamatayo anati, "Amayi, mukuchita ngati anthu amenewo," nati, "chifukwa chiyani, motani!"

Mayiyo anati, "Chabwino okondedwa, ndimangoganizira."

Nati, "Mukuganiza chiyani?"

18 Nati, "Ngati Mulungu anandichiritsa ndi gawo la Mawu osazodzedwa, angachite motani ndi amene ali ozodzedwa?"

19 Tsopano, Tilola wosuma mulandu aitane mboni zake, woyambirira kuima, apereke umboni wake.

20 Ndangonena maminiti apitawo, chifukwa ndimawerenga pamene ndimawerenga pomwe Scofield akunena kuti Mawu ena sakupezake mu mabukhu ena. Pamenepo ndipo pakuchokera nkhani yonsezi. Koma ziri motere.

21 Tsopano Bambo Kusakhulupirira aima, napereka umboni wao motsutsana ndi Mawu a Mulungu. Ndipo tsopano pamene iwo...Iwo ndi mboni yoyamba kuima. Ndiye tikupeza kuti pamene alumbirira, chodandaula chawo ndi ichi "Malonjezo a Mawu a Mulungu sali owona kwathunthu."

22 Tsopano mboni zonsezo zimene wosuma mulandu wabweretsa zikuti iwo ndi anthu okhulupirira. Onsewo akuti ndi wokhulupirira ndipo akupeleka umboni woti, "Sitikanakhala nawo pa misonkhano, tikanakhala kuti siife okhulupirira." Ndiye iwo - akunena kuti ali okhulupira.

23 Ndiye chodandaula chimene Bambo Kusakhulupirira akupeleka umboni motsutsana ndi Mawu a Mulungu akuti, "Marko 16 ndi zabodza, sizingakhale zoona." Chifukwa akuti iwo anadwala nthawi ina, "adapita ku misonkhano ya anthu odzitchula kuti ali ndi Mzimu Woyera, kumene anawasanjika anthu manja ndikumanena kuti achiritsidwa." Ndiye adapita pamzere wa anthu opemphereredwa, ndipo pamene anatero...Anali atadwala kwambiri kwa kanthawi,

ndiye "adapemphereredwa ndi anthu a Mzimu Woyera (odzitcha kuti ali ndi Mzimu Woyera) amene amafuula ndi kuchita phokoso, ndi kumati achiritsidwa." Tsono Bambo Kusakhulupirira anayenda mumzere umenewo, nasanjikizidwa manja, "Imeneyo inali miyezi iwiri yapitayo; ndipo palibe chisonyezo chirichonse cha kuchira." Ndiye anati, "Pamenepo Mawu a Mulungu pa gawo limeneli sali owona."

24 Tsopano wosuma mulandu akhazika pansi mboni yake yoyamba, naitana mboni yake mboni yake yachiwiri, yomwe ndi Bambo Kukaikitsa. Akulumbirira natenga mbali yake. Tsono iyeyu akuti ndi wokhulupirira, ndipo iye "anamva kuti. Mumzindawo munali tchalitchi, kumene anali ndi mbusa wokhulupirika, otchedwa munthu wa Mulungu, momwe anthu opemphera ankanenera. Ndipo munthu ameneyu akuti anakhulupirira Mawu a Mulungu. Ndipo anapempherera odwala, nawadzoza mafuta. Ndipo anawerenga awu a m'Baibulo pa Yakobo mutu wa 5 ndime ya 14, 'Kodi pali odwala wina pakati panu? Kauzeni akulu ampingo, ndipo amudzoze mafuta nawapempherere, pemphero la oyeramtima lidzawachiritsa, ndipo Mulungu adzawadzutsa iwo!'" Tsopano akunena kuti anapita kumeneko akudwala kwambiri madotolo atamulephera kumuchiza malungo amene anali nawo. Ndipo Dotolo anati matenda amenewo sadzatha, panalibe njira yoti adzathere. Tsono iye "Anamvera Mulungu pa Mawu ake," ndipo iye "anakapeza uyu wotchedwa mbusa wa umulungu," kumene mpingo wonse unali ndi maumboni amitundu mitundu onena kuti anachiritsidwa ndi zina zotero. Ndipo mbusa wa umulungu uyu anamupemphera, namudzoza mafuta, molingana ndi Mawu a Mulungu. Iye sanakaikire kutsimikiza mtima kwa munthuyo, sanakaikire kutsimikiza mtima kwa mpingowo; Ndipo mbusayo anatenga ndondomeko monga mmene Mawu a Mulungu akunenera, namudzoza ndi kumupempherera. Izo zinachitika kopitirira miyezi isanu ndi umodzi tsopano koma panalibe chisonyezo chakuchira. Motero anapereka umboni umenewu. Tsopano mboni yachiwiri anakhala pansi.

25 Wosuma mulandu abweretsa mboni yake yachitatu, Bambo Kusapirira Iyeyu aima, nalumbira kuti apereka umboni motsutsana ndi Mawu a Mulungu, kuti sali owona. Munthu ameneyu akudza nanena kuti Iyeyo ndi okhulu-

pirira, ndipo akuti anawerenga tsiku lina pa Marko 16 kapena titi pa Marko 11, kuyambira vesi 22, Pamene Yesu Mwiniwake...Iyeyo akuti anali ndi Baibulo lija lolembedwa malo ena ndi inki yofiira ndipo mawu ofiirawo ndi mawu eni eni olankhulidwa ndi Yesu Mwiniwake. Ndikuti mu mawu ofiirawo pa Marko 11, pamene Yesu akulankhula, anati, "Khulupirani Mulungu. Ndithu ndinena ndi inu kuti munthu akanena ndi phiri ili, nyamuka nuponyedwe mnyanja, wosakayika mumtima mwake koma nakhulupirira kuti chimene achinena chichitika, adzalandira chomwe wanena". Ndipo anati, "Iyeyo anali wopunduka," nati, "kwa zaka zambiri", kuyambira akali mnyamata. Wakhala ali wolumala mapazi ache. Ankayenda ndi ndodo. Tsono anavomereza kuti pokhala Mawu a Mulungu ndi osasinthika, anati mumtima mwake monga mmene amachitira umboni tsopano, nati, "ndidzayenda." Anabvomereza Mawu a Yesu Khristu, nati adzayenda chifukwa Yesu anatero. "Ngati unena kwa phiri iri 'nyamuka' ndipo pamene uvomereza, pamene ukupemphera khulupirira kuti ulandira chimene unachipempha, ndipo udzakhala nacho. Ndipo iye anapemphera, icho napemphera icho, nati 'adzakhala nacho,' ndipo izo zinali zaka zisanu zapitazo." Ndipo adakali olumala pa mapazi ake, sanachiritsidwebe.

26 Tsopano wosuma mlandu abwera zitatha mboni zake kupereka maumboni ochokera Mbukhu Lopatulika (monga achitira mu bwalo la milandu ya Chiyuda ndi umboni) amakhala ndi mboni zitatu monga mwa Malembo momwe analemba mu Baibulo la Mulungu "mongoyerekeza Yesu ananena," amene ali mwana wa Mulungu. Mulungu anapanga thupi, nakhala mwa munthu, wodalilikayo. Ndipo wozenga mlandu adzano nadzatsimikizira mlanduwo kwa inu anthu. Tsono mukumbukire kuti ndinu othandiza pa mlandu umenewu ndiponso ndi oweruza ake.

27 Kotero wosuma mlandu akufuna mumvetse pamene akutsimikiziranso umboni uja kuti mboni zija zikuti iwo ndi okhulupirira, monga mmene onse aiwo akudzitchulira, kotero iyenso akufunsa wosuma mlandu, akufuna kuti inu mudziwe kuti "Mulungu sali wolungama chifukwa anapereka malonjezo opanda pake ngati amenewa, mu Mawu Ake, pamene Iye samawakwaniritsa, ngakhale wazipereka izi kwa ana Ake amene akuti okhulupirira.

Ndipo pakuvomereza zimenezi amachita manyazi ndi kutinso akuchititsidwa manyazi ponena Mawu amene sali owona." Wosuma mulandu tsopano akuti, "chifukwa Walephera kukwaniritsa malonjezo kwa mboni zitatu zija, zimene zakamba bwinobwino mogwirizana ndi Mawu a Mulungu." Ndipo wosuma mlanduyu akufuna kuti inu mudziwe kuti, "Mulungu walephera, kwa milandu itatu yonse ija kuwonetsa chikwaniritso pa kusunga kwa Mawu Ake." (akutsimikizira izi kwa inu) ndi kwa mboni zitatu zimene zikuti zimakhulupirira.

28 Tsopanonso, wosuma mlandu akufuna kuti mumvetse china chake. "Iye amene ali Mulungu, analonjeza kuti zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira. Analonjeza zimenezo." Wosuma mlandu akufuna kuti mudziwe zimenezo. Ndipo anthu awa odzitcha okhulupirira ayesa kusunga Mawu amenewa, koma Iye akulephera kusunga mawuwo, kotero Iye akuzengedwa mlandu wakuswa lonjezo.

29 Komanso wosuma mlandu akufuna mumvetsenso Mawu ena a Mulungu. "Iye akuti ndi wamoyo koma atafa kale." Wosuma mlandu akufuna kuti inu mudziwe kuti iye sanawone munthu wokhala ndi zipyera za misomali m'manja mwake, ndi zipyera mthupi mwake monse ndi momwe anabooledwa ndi misomali m'mapazi ake. Ndiponso sanawonepo chisoti cha minga pa mutu wa wina aliynse, koma iyeyu akumati ndi wamoyo pamene anafa kale. Ndiponso amanena kuti pa Aheberi 13:8 kuti ali wa moyo. Koma siziri choncho. Amanenanso pa Luka Mutu wa 17 ndime ya 30. Kuti masiku, ano amene tikukhalamo tsopano adzadzulula yekha; ngati mmene analili mmasiku amenewo, ndi mmene adzakhalire. Akunenanso choncho, wosuma mlandu tsopano apeleka mlandu momveka kuti pa chi vumbulutso 10, akuti mngelo wa chisanu ndi chiwiri, pamene adzayamba kuwomba (ameneyo ndiye - ndiye mngelo waku mpingo wa Laodikaya amene ayenera kuyitanira mpingo ku chikhulupiriro cha atate), "kuti pamene mngelo akuwomba zinsinsi zonse za Mulungu zidzaululidwa patsiku limenelo. Ndiponso akuti pa Malaki 4 kuti aneneri oyera ananenera kuti adzakonze zinthu izi kuti zikhale zooni. Komano palibe choona cha zonsezi! Akunenanso kuti kumwamba ndi dziko lapansi zidzachoka koma Mawu Ake sadzalephera kukwaniritsidwa.

30 Tsopano wosuma mlandu ali ndi mlandu pano. Iye akuyesetsa kulongosola. Ndiye akupereka mlandu kwa bwalo kwa inu amene muli nduna za pa mlandu ndi oweruza mlandu. Tsopano tamva mbali imeneyi, tamva mboni zonse. Tamva zonse zimene anena pa nkhaniyi. Tamva zimene wosuma mlandu waonjezera pa Mawu momveka ku mbali zonse, "Malonjezo onse amene Mulungu anapereka, koma palibe chirichonse cha zimenezo," chimene wachiona kuti "Ndi Choonadi." Koterok akuyesetsa kupeza mulandu wotsutsa Mulungu, ndi kutsutsana opanga malonjezo opanda pake ngati amenewa, chifukwa malonjezo amene Mulungu anapereka ndi opanda pake kwa ntheradi. Malonjezo amene Mulungu anapereka okhuza masiku ano ndi opanda pake kwa ntheradi. Ndipo Iyeyo samawasunga! Tsopano tamva mbali yake, tsono tiuze wosuma mulandu ndi mboni zake kuti akhale pansi.

31 Ndipo tsopano tikuitana mboni yotchinjiriza mlandu kwa wozengedwayu. Ndipo tsopano wotchinjirizira ndi Mzimu Woyera, Iye tsopano adza naima mmalo mwa wozengedwa mlanduyo. Tsopano choyamba chimene akufuna ndicho kuti bwalo likhale tcheru, haleluya, kuti wosuma mulandu sakutanthauzira bwino Mawu a Mulungu kwa anthu, monga m'mene anachitiranso kwa Hava pachiyambi. Kumbukirani, Iye anali ameme amatanthauzira kwa Hava. Mulungu anawauza zoyenera kuchita, ndipo sikukanadzakhala imfa, chisoni, kapena chirichonse, ndipo iye anadza ndi kudzatanthauzira mosiyana ndi Mawu. Koterok pamene munthu achoka pa Mawu a Mulungu chimachitika ndi chiyani? Iye sangatchinjurizedwenso ndi Mulungu. Koma mukuwona, Satana anali amene anatanthauzira Mawu kwa Hava. Iye sadamvere mwamuna wake ndi Mulungu, koma iye adatenga mawu a wosuma Mlandu. Ndipo iye alibe ulamulirowo watanthauzira ndiponso munthu aliyense alibe ulamulirowo. Mulungu amatanthauzira yekha Mawu Ake. Iye samasowa ife; Iye amasunga Mawu Ake, tikukhulupirira. Tsopano akufuna kuti mukhale tcheru pa chimenecho kuti amene anatanthauzira Mawu oyamba amene Mulungu analankhula, ndi wosuma amene akuyesa kuti - kuti abweretsa mulandu pamaso pa bwaloli masana ano, mofanananso ndipo wamasulira mopotoza Mawu. Chimenecho ndicho choyamba chimene mboni akufuna kunena. Tsopano, akufuna kuti mumvetsetse, kuti iye anali womasulira mawu kwa Hava

koma anamasulira mopotoza.

32 Malo oyamba, Iye akufuna kukupatsani chiganizo ichi, kuti lonjezo ili liri kwa okhulupirira okha; osati odzipangitsa kukhala okhulupirira, okaikitsa, kapena osakhulupirira. Ndi za iwo okha amene akhulupirira: Tsopano akufuna bwalo ili...Wotchinjiriza Mulandu (Mzimu Woyera) akufuna kuti bwalo lizindikire kuti malonjezo ali kwa okhulupirira okha.

Ndiye pofunsidwa iye anati, "Awa ndi okhulupirira!"

33 Ndipo tsopano Wotchinjiriza Mulandu Yekha ayenera kudziwa ngati ali okhulupirira kapena ayi, chifukwa Iyeyo ndi amene amakwaniritsa lonjezo. Tsono mudutsa bwanji zimenezo? Muli nazo zambiri...Mulandu wabvuta. Mudutsa bwanji zimenezo? Mzimu Woyera ayenera kudziwa, chifukwa Iye ndi moyo umene uli mu Mawu, Iye ndi amene amafulumizitsa Mawu. Monga m'mene mzimu wanu umafulumizitsa thupi lanu, ndipo thupi limafulumizidwa ndi Mzimu. Popanda Mzimu thupi liribe kanthu, thupi ndi lakufa. Ndipo Mawu ndi akufa popanda Mzimu. Zimatengera Mzimu kubweretsa mawu kuti akhale ndi Moyo. Ndipo Iye ndi wofulumizitsa Mawu, ndipo ndi Mboni ya Wotchinjiriza Mulandu. Amen. Kodi mudutsa bwanji pamenpo? Ndikufuna kuti bwalo limvetsetse chimencho bwino bwino kuti iye ndi Wofulumizitsa, ayenera kudziwa. Amafulumizitsa Mawu.

34 Ndibwerezanso, Iye akufunsa kuti bwalo litchere makutu ku Mawu a lonjezo limene liri pafunso. Mulungu sanaike nthawi yoti iwo adzachirire. Iye anati, "Pemphero la chichulupiriro lidzapulumutsa wodwala, ndipo Mulungu adzawadzutsa iwo." Sanati "pomwepo." "Adzaika manja awo pa odwala ndipo adzachiritsidwa." Sanati "tsiku limodzi mwezi kapena chaka." Iye anangoti, "Adza!" Mboni Yotchinjiriza Mulandu ikufuna kuti mudziwe zimenezo, kuti Iye sanati padzakhala chodabwitsa. Anangoti "Adzachira!" Tanthauzirani Mawu bwino. "Adzachira!" Sanayike nthawi yake. Ndiye kuti, ngati ali okhulupirira adzachira. "Adzaika manja awo pa odwala ndipo adzachira," kaya tsopano ndi mlungu umodzi, mwezi, chaka, zaka khumi, zaka makumi awiri, zaka makumi asanu. "Adzachira," Anatero! Apo ndi ngati angakhalebe

ndi chikhulupiriro chao. Tsopano, umenewo ndi umboni wa Wotchinjiriza mlandu.

35 Chinthu chinanso, mboni Yotchinjiriza mlandu akufuna kuti bwalo litchere makutu masana ano, kuti Mawu ndiwo Mbewu, ndikuti mbewu iyenera kugwera panthaka yachonde kuti ikafulumizidwe. Mbewu singathe kumera pa mwala. Mbewu iyenera kupeza chonde Ndipo Mawu ayenera kugwera pa' chikhulupiriro, chimene chiri chonde chimene chimapangitsa Mawu kuti akwaniritsike. Tsopano mboni Yotchinjiriza mulandu pa nthawi ino...

36 Tikanakhoza kutchula zinthu zambiri, zinthu zikhoza kunenedwa. Koma sitikufuna kuti tikukhazikeni nthawi yaitali, tiri ndi mzere waukulu wa anthu ofuna kupemphereredwa. Ndikufuna inuyo, bwalo, kuti mumvetsetse.

37 Mboni Yotchinjiriza Mulandu tsopano ali ndi mwayi woyitana mboni chifukwa wosuma mulandu pa nthawi yake anaitana mboni. Tsono wotchinjiriza Mulandu aitana mboni. Ndipo wotchinjiriza mulandu akufuna kupereka kwa bwaloli, masana ano, mneneri Nowa, "Idzani kutsogolo kuno a Nowa ndi kudzayima. Tsono ndikumva kuti muli ndi umboni wokhudzana ndi Mawu a Mulungu amene anapatsidwa kwa inu.

"Inde."

38 Mboni lero ikufuna kunena, kwa bwalo lino, kuti iyeyo anali munthu wamba ndipo anakhulupirira Mulungu. Ndipo anakhala mu mbadwo wa sayansi pamene anthu anakhulupirira kuti masiku a zozizwitsa kunalibe. Kunali kusanagwe mvula pa dziko lapansi koma tsiku lina anakumana ndi Mulungu. Ndipo Mulungu anamuza kuti aseme chombo choti adzapulumu tsiremo anthu, ndi kuti onse adzabwere ku chombo kuti adzapulumutsidwe. Ndiye mboniyi ikufuna kunena kuti Iyeyo mokhudzidwa ndi mtima wake wonse, anakhulupirira. Ndipo anapita nakazilalikira. Napita osati kukangolalikira kokha koma, kuti ntchito yake ichitire umboni za chikhulupiriro chake, anayamba kumanga chombo.

39 Ndipo mboniyo ikufuna koloza chala kwa Bambo

Kusakhulupira ndi Bambo Kukaikitsa ndi Bambo Kusapirira. "Iwowa anali kundivutitsa usana ndi usiku. 'Mvula ija ibwera liti? Ha, siunanena chaka chapitacho, koma kulibe mvula kumwambaku. Tinapita kwa anthu a sayansi ndipo atsimmikiriza kuti kulibe mvula kumwambaku.' Ndipo anakanena kuti ine ndine wopenga. Ndipo anandinyodogola nandiuza kuti ndinali 'wopusa ndi chinzete kwathunthu pokhulupirira lonjezo lokhala ngati limeneli, motsutsana ndi wofufuza mwa sayansi.' Koma Iye anati, "Ndinagwira ntchito mwa dongosolo, chifukwa ndinayima mosagwedezeke chifukwa ndinadziwa kuti anali Mawu a Mulungu ndipo sangalephere. Ndinamangabe chombo."

40 Chitatha chombo, anthu onyogodola anathamanga mozungulira chombocho tsiku ndi tsiku, pamene ine ndinayima pakhomu kuwalalikira. Iwo amanenabe kuti 'Tsopano, papita zaka zana ndi makumi awiri, nanga mvula yako iri kuti? Kotero waona, ntchito yako yonse ndi ya chabe,' anati, 'Asayansi anthu, ali oona, ndipo palibe chinthu chokhala ngati chimenechi. Ndipo iwe chabe ndi okalamba, pakukhukupirira lonjezo lopanda pake ngati limenelo.'

41 Tsopano linafika tsiku pamene ine ndinali kuyenda m'mawa wina, kunja kwa chombo changa. Tsono, mwa dzidzidzi, popanda dzanja, chitseko chinatsekeka pa nkhope panga ndipo ndinamatidwira mkati, 'Tsopano chinachitika ndi chiyani?' Tsono ine ndinakwera makwerero amene ndidamanga, ndinakwera pamwamba ndi kutsegule zenera. Ndipo ndimakhoza kumamva panja; Bambo Kusakhulupirira atakhala pamenpo, Bambo Kukaikitsa ndi ndi Kusapirira akuti, 'Tsopano chachitika nchiyani? Wadzitsekedwa yekha!' Ndinaganizira zoonza kuti mvula iyenera kugwano. Ndipo tsiku limene ndinalowa linali pa 27...kapena pa 17 mwezi wa Meyi. Chitseko chinatsekeka pa maso panga Ndinayitana anthu anga pamodzi ndikunena, "Konzekani, mvula iyamba kugwa mu mamniti ochepa." Ndipo tsiku lonse lathunthu Bambo Kusakhulupirira ndi Bambo Kukaikitsa ndi Bambo Kusapirira anayenda yenda mozungulira chombo changa kumatsutsa ine ndi kundinenera zinthu zoipa. Koma ndinauza anthu anga 'Khalani chete, Mulungu analonjeza!'

42 Tsiku lachiwiri, dzuwa linatuluka lowala; kopanda mvula, kopanda bingu ndi kopanda mphenzi. Tsiku lachitatu chimodzimodzi, Tsiku lachinai, lachisanu lachisanu ndi chimodzi. Koma mmawa wa tsiku la 24 Meyi (zaka 120 zitatha), madzi anakhuthuka kuchokera kumwamba. Ndipo iwo onse odzozedwa ndi Bambo Kusakhulupirira, Kukaikitsa ndi Kusapirira anawonongeka panja paja."

43 Mboni Yotchinjiriza mlandu inati, "Khalani pansi a Nowa. Ndikufuna kuitana mboni yina. Tayimirani a Bambo Abrahamu, ndikufuna kuti mutipatse umboni."

44 Bambo Abrahamu adza, nati "Ine ndinkagwira ntchito pa munda wanga kunja kwa mzinda wa Uru, mdziko la Akaldia. Ndipo ndinali nditakwatira nsuweni wanga dzina lake anali Sarai ndipo ine ndidali kutchedwa Abram. Ndipo ndinakumana ndi Mulungu, ndipo Mulungu anandiuza kuti ndidzakhala ndi mwana kupyolera mwa Sarah. Ndipo Sarah panthawi imeneyi anali wa zaka 65 ndipo ine ndinali ndi zaka 75. Ndipo Mulungu anandiuza kuti ndidzakhala ndi mwana kupyolera mwa Sarah, ndi kuti kupyolera mwa mwanayo dziko lonse lidzadalitsika, ndipo ine ndidzakhala atate wa mafuko. Mofulumira ndinabwerera, ndinabwerera, chifukwa cha chimwemwe chimene chinali mumtima mwanga. Ndinkakonda ana nthawi zonse, ngakhale ndimaganza kuti sindidzakhala naye mwana konse. Kome pamene Mulungu ananena kuti ndidzakhala naye, ndinamukhulupirira. Ndinapita kwa dotolo kuti tikagwirizane za chikonzekero. Iye anandithamangitsa mu ofesimo. Bambo Kusakhulupirira anali atakhala momwemo. Ndipo ndidapita ku msewu, ndipo anthu aulamuliro anafuna kundimanga chifukwa amaganiza kuti ndachita misala. Ndipo pamene zaka zinapitapo. Bambo Kusapirira anasautsa ine usana ndi usiku.

45 Mwezi woyamba ndinati kwa mkazi wanga Sarah. Onani iye anali atapitirira nthawi ya kuvutika kwa akazi, zinatha kwa iye monga achitira akazi. Ndipo ndinati kwa Sarah, 'Okonedwa kodi tiri ndi tinsapato toluka ndi matewera ndi - ma - ma - mapinifolo? Takonzekera sichoncho?' 'Inde takonza zonse.' 'Zichitika tsopano, ingodikira uone.' Ndipo kumapeto kwa masiku 28, ndinati

'Ukupeza bwanji wokondedwa?' "Palibe kusintha, Abrahamu." Chabwino anati, "Ndinati, Ambuye adalitsidwe! Sarah, usakaikire. Mulungu anatero kuti tikhala naye mwa njira ili yonse!" Izi zinapitira kwa zaka zingapo.

46 Ndipo chaka ndi chaka zitapita Bambo Kukaikitsa, Bambo Kusakhulupirira onse aiwo ankandiseka ine. Koma zaka makumi awiri ndi mphambu zisanu zitapita, mwana anabadwa pamene ine ndinali ndi zaka 100. Mulungu sanandiuze ine kuti ndidzakhala ndi mwana tsiku linalo. Iye anangoti ndidzakhala naye! Ndipo ine sindikudandaula kuti zinatenga nthawi yaitali bwanji, Mulungu analonjeza! Ine ndinadikira zaka 25. Iwo ankaganiza kuti ndidzakalamba ndi kufa, koma ine ndinati, 'Sindingafe, lonjezo liri kwa ine. Mulungu anatero!'

47 "Ndipo mmene Bambo Kungyoza, Bambo Kusakhulupirira, Bambo Kukaikitsa, Bambo Kusapirira, ankangobwerabwera, iwo anawadzodza anthu, namati, 'Abrahamu muli ndi ana angati tsopano, atate wa mafuko, amene muli nawo?' Koma ine ndinaima mosatekeseka, chifukwa sindimagwedezeke pa Mawu a Mulungu chifukwa cha kusakhulupirira. Ndinadziwa kuti Mulungu akhoza kusunga Liwu liri lonse limene analilonjeza. Sindinaganizire za thupi langa kuti ndi lakufa kapena kuuma kwa mimba ya Sarah. Koma ndinakhulupirira Mulungu. Iwo anati, 'Chabwino, ndimaganiza kuti unanena zaka 25 zapitazo, kuti udzakhala ndi mwana?' 'Ndinanenadi zaka 25 zapitazo' Koma Bambo Kusapirira pamenepo anati, "Chabwino, zaka 25 zapita, tikuwonerani tsopano! Ndevu zafikano pafupifupi m'mabondo anu. Tawonani mwakalamba tsopano." Ndinamuuza kuti Mulungu sanandiuze nthawi imene ndikanayenera kukhala ndi mwana ameneyu. Iye anangoti, 'Udzakhala naye kupyolera mwa Sarah;' ndipo ndizokhazikika basi! Ine ndinagwiritsitsa zimenezo. Tsopano Mawu sananene kuti ndi liti, koma anati zidzachitika!"

48 Tiyeni tiitane mboni yina mofulumira, tiribe nthawi yokwanira, tikanakhoza kuitana 100 aiwo. Tiitane mboni yina tsopano, Mose, apereka umoni.

49 "Mukudziwa," iye anati, "Ine ndinaphunzitsidwa mu

nzeru zonse za Aigupto. Ndinali mphunzitsi woposa ena onse. Koma tsiku lina ku chipululu, ndiri ndi zaka 80. Ndinakumana ndi Mulungu. Ndipo anali m'ma onekedwe a-a-chizindikiro, ndipo Iye anali moto woyaka mu chitsamba. Ndipo Iye-Iye anandiuza kuti anamva ku dandaula kwa anthu Ake, ndipo anakumbukira, lonjezo lake lowapulumutsa. Ndipo anati "Ndikukutuma iwe." Ndipo ndinati, 'Ndine yani ine? Sindingathe kulankhula bwino. Ine-ine-ine sindine-ine sindiri-ine sindiri wophunzira za chipembezo sindi-sindingapite!' Iye anati, "Udzapatsidwa zizindikiro ziwiri. Chimodzi cha izo chidzakhala m'dzanja lako ndipo china chidzakhala mu ndodo. Ndipo ngati sakamvera mawu a chizindikiro chimenchi, ukathire madzi pansi, adzasandulika mwazi, ndiye chimencho chidzatsiriza zonse."

50 Pamene ndinatenga chizindikiro chimene Mulungu anandipatsa ndinapita pamaso pa Farao, Mbusa Farao, iye anayesa kuitenga mphatso yanga ngati yachabechabe. Anati "Ambiri amatsenga kapena Aigupto angathe kuchita zimenzo. Pafupifupi wamatsenga aliyense akhoza kuchita matsenga awa." Ndipo anakatenga, amuna awiri maina awo ndi Ayane ndi Ayambre ndipo anachita moonera chirichonse chimene ndinkachita. Koma izo sizinandigonjetse ine chifukwa Liwu limene linandituma ine linali Liwu logwirizana ndi Malembo, ndipo ndinalimba mtima. Linali Liwu la Mulungu.

51 "Chinali chizindikiro chogwirizana ndi Malembo ndi Liwu la mwa Malembo, 'chifukwa ndakumbukira lonjezo Langa ndipo nthawi yakwana.' Analibe anerei mu Israeli kwa mazana, zaka 440 analibe aneneri mu Israeli koma Iye anati, 'Ndikukutuma kuti ukhale iweyo.' Ndipo anapita. 'Ndipo anandiuza kuti, kuti chikhale chizindikiro, ndidzabwera ndi ana ku phiri ili.' Zinatenga nthawi yaitali koma ndinazichita, ndinakhazikika moona pa Mawu. Ndipo pamene Ayambre ndi ena ochita moonera mwa chithupithupi anayesa kunyogodola, koma ine sindinadandaule chirichonse kuti akundinyogodola bwanji ..."

52 Kodi mukudziwa kuti zimenezo zibwerezanso m'masiku otsiriza? Yesu anatero. Baibulo linati, "Monga Ayane ndi Ayambre anatsutsana ndi Mose momwemonso anthu awa m'masiku otsiriza," owonera kumangochita

ngati kutsanzira.

53 Koma anati, "Ine ndinayima nji chifukwa ndinadziwa Liwu lija linali logwirizana ndi Malembo." Koma iwo anali anthu awiri, koma uyu m'modzi yekha. Ndipo anapita kumunsi ndipo anakachita zimene iye...ndipo ana, zinakwaniritsidwa kuti zake ndi zoona, nadzadzera kuphiri komweko kumene Mulungu adamuza.

54 "Khala pansi, Mose. Tiyeni tiitane mboni yina msanga. Yoswa."

55 Yoswa anati, "Pamene tinali kuyandikira kudziko, tinafika ku Kadesh-Barnea. Ndipo Mose, wantchito wa Mulungu anapita, anapita nakatenga aliyense...mmodzi, pa fuko liri lonse, munthu mmodzi wa gulu, ndipo anati, 'Tiyeni tikwere ndipo tikaone dzikolo.' Ndipo tinapitako, awiri a ife, ndipo tinabwerako ndichitsimikizo kuti dziko linali labwino." Iwo anali ndi umboni wa dzikolo. Iwo adali Apentekosite enieni. Ndipo anabwerako ndiumboni woti dzikolo ndilabwino. Koma pamene inakwana nthawi yakuti akatenge dziko lonselo anati, "Sitingathe. Sitingathe. Ndife osayenera." Ndipo anthu onse adasokonezeka, sanadziwe chochita, ndi gulu loti avomerezane nalo. Ndipo ine ndinawatontholetsa ponena kuti, "Kumbukirani, ndilo njezano la Mulungu!" Mulungu anati, "Ndikupatsani dzikoli." Ndipo chimene Mulungu alonjeza, amachichita!" Ndinawathanoletsa anthuwo, Tsiku linalo, anati, 'Kodi tidzapita liti?' Tsiku linanso, 'Kodi tipita lero?' "Padapita zaka makumi anayi, komabe tinadzatenga dzikolo!"

56 Mboni yina yimodzi, mofulumira lekani ndiitane Yesaya ayime. "Yesaya, Ungaperekere umboni kwa Mboni Yotchinjiriza, ndikutipatsa chotsutsa kwa osumawo, Wotsutsana naye?"

57 "Ndipereka. Ndinali mneneri. Ndinali mneneri wotsimikizika. Chimene ndidanena, sanachi...Ine - sindinkadziwa zimene ndinali kunena, koma Mulungu anachititsa zomwe ndinkanena kuchitika. Aliyense anayamba kuzikhulupirira, mpingo wonse adayamba kuzikhulupirira. Ndipo tsiku limodzi chinthu chachilendo chinachitika. Ambuye Mulungu adati kwa ine, 'Israeli akufuna zizindikiro, ndipo Ine ndikufuna iwo apange

zimenezozo, koma ndidzawapatsa chizindikiro Chapamwamba. Ndipo icho chidzakhala cha mbadwo wa pamwamba pamene ali ndi misika yapamwamba ndi ndege zapamwamba ndi zapamwamba, chirichonse chapamwamba. Ndidzawapatsa iwo chizindikiro chapamwamba, namwali adzaima! Ndipo ine pokhala mnereri wotsimikizika, namwali aliyense anasokeratu tinsapato take, ndi zina zotero, 'adzakhala ndimwana, inde bwana,' anali, 'yemwe Yehova anamwitana.' Zinthu zambiri zotero zinachitika. Inde, bwana, 'Chabwino koma ife tikumdikirira mwana wathu, msungwana wathuyu kuti akhale ndipakati.' Aliyense ankaganiza za mwanayo. Msungwana aliyense ankayembekezera mwanayo. Zaka zidapita. Ena a iwo anakanda kumutu kwawo, nanena, 'Mneneri wokalamba uja ndi wonyenga.' Koma zinadzachitika zakamazana asanu ndi atatu zitapita. Mulungu sananene kuti ndiliti ati adzaima, Anati adzaima! Zitapita zaka mazana asanu ndi atatu anadzaima."

58 Tsopano kwa mboni yomaliza, ngati mungandikhulukire, kodi ndingakhale mboni yomaliza? Izino siziri mu Baibulo, ndi za masiku ano. Lekani ndikhale mboni yina, pakanthawi tisanayambe mzere wopempherera odwala. Ndipo mvetsetsani kwambiri. Ndifuna ndipereke umboni wa za Iye. Ndifuna, kuitanidwa ndiime, ndikuimika mkono kuti ndinene Zoona, sichina koma Zoona.

59 Ndifuna ndinene, kuti ndinakhala Mkristu motani? Atate ndi amayi wanga, agogo aamuna, agogo aakazi a makolo anga onse anali ochimwa. Ndipo chikhalidwe changa chinali cha nansongole...ndipo ngati ine ndiri mbewu ya tirigu. Koma tsiku lina mmawa mkanyunba kamatabwa kaja ku Kentucky, amayi anga ndi anamwino akutero kuti mmwezi wa April pa 6, mmawa nthawi ya 5 koloko. Mchaka cha 1909, pamene Ambuye Mulungu anandifikitsa mdziko lapansi kunadza Kuwala kudzaima pakazenera kakang'ono. Ndipo pamene anatsegula zenera amayi atagona pakabedi ka mauzu pofuna kudziwa kuti ndi mwana wotani amene ali naye, Kuwala kunalowa mkatimo. Ndipo anthu akumapiriwo sanathe kuganiza kuti adziwe kuti ndichiyani. Ndinali mwana kwambiri kuti ndidziwe.

60 Ndipo ndiri mwana, wa zaka zisanu ndi zitatu, zisanu ndiziwiri kapena ndi zitatu ndinali kutunga madzi odzathira pa dziwe limene abambo anga anali nalo. Ndipo madzulo ena mwezi wa September kukufunda, ndinakhala pansi, ndikulira popita ku dziwe ndi anzanga kukaweza nsomba ndipo iwo...ndinalephera kupita nawo chifukwa, ndinayenera kupita kukatunganso madzi. Ndinamva ngati Kamvulumvulu mumtengo, m'mwamba pang'ono. Kunali ku Indiana mu September, zonse ziri bata ndithu, kungoti zii ngati zonse zafa. Ndipo mu kamvulumvulu uyu amene anali pakathengo munachokera Liwu ndipo linati, "Usadzasute, fodya, usadamwe mowa, usadzaononge thupi lako (uko nkuyenda ndi akazi) chiri chonse chotero, pakuti pali ntchito yoti udzaichite ukadzakula." Ndipo amayi wanga adaitana a dotolo, ankayesa kuti ndasokonezeka.

61 Patapita sabata imodzi, ndinaona, zitatha izi Mulatho wa Municipal, M'masomphenya monga dzina lomwe ine ndinkawutcha, ndinauwona Mulatho wa Municipal ukumangidwa pa Mtsinje wa Ohio, ndinaonanso amuna khumi ndi asanu ndi mmodzi akutaya miyoyo yawo pamenepo. Patapita zaka makumi awiri ndi mphambu ziwiri kuchokera pa tsiku limenelo, Mulatho wa Municipal unayamba kumangidwa pa malo omwewo ndipo anthu khumi ndi asanu ndi m'modzi anataya miyoyo yawo pamenepo.

62 Ku Mtchini wa a Green, usiku wina posadziwa kuti ichi chinali chiyani...Pambuyo pake ndinadzakhala mtumiki wotumikira Ambuye. Ku Mtchini wa a Green usiku wina...Azibusa anga anali atangondiuza...ndimakhoza kuwauza iwo, pokhala...pokhala kuti ndimakhoza kuwona zinthu adandiuza kuti ndi za Satana. Ndipo ine pokhala Mkristu, sindinafune kuyanjana naye Satana, m'nena mpang'ono pomwe. Kotero ndidapita uko, ndinati, "Ambuye, sindingalole...kuyenda m'moyo woterowo." Ndipo ndinangokhala pa kamalo kumeneko mbali ya kuja komwe anthu amasodza, ndikupemphera. Ndipo usiku umodzi komweko, ndi pomwe Ambuye analankhula nane' ndipotu pamtengo, momwe anachitira kwa Mose. Ndipo apa pa Mtchini wa a Green, kunadza mwamuna mkatimo nandiuza kuti, ndisamapemphe kuti andichotsere Ichi koma ndidziwe kuti inali mphatso yochokera kwa Mulungu imene inayenera kugwiritsidwira ntchito kwa anthu a m'dziko

lonse lapansi nandifotokozera mwa Malembo kuti zonsezi zinalonjezedwa mu Baibulo ndipo ziyenera kukwaniritsidwa, pakuti nthawi yayandikira.

63 Ndipo ndinabwerera ndi kukawauza abusa anga. Ndinapita kukawauza, ndipo iwo anati, "Billy, Kodi wadyanji? Kodi umalota, kapena umabwebweta kutulo?" Koma kwa ine, zinali Malaki 4. Iwo anati, "Ndiye utanino?" Zinali Luka 17:30. Zinalinso Chivumbulutso 10. Zinali Malembo ena onsewa amene analonjezedwera ku masiku otsiriza. Sindinawone kuti zikuyenda bwino. Anthu ankadabwa kuti, "Chimenechi chidzachitika liti?" Koma ine ndinangogwiritsitsabe.

64 Tsiku lina pamtsinje, ine ndinali kubatiza anthu 500 ku mtsinje, pamene mwadzidzidzi, Kuwala komwe kuja kumene kunadza kwa ine ndiri ka mnyamata kakang'ono. Ndipo ndinali nditawauza anthu kuti ndinkakhoza kukaona. Iwo ankati ine ndinkangolota ndi kuti mwina ndiri ndi mutu waukulu. Koma pamaso pa anthu zikwi zisanu, nthawi ya 2 koloko madzulo, m'chaka cha 1933, Mtambo umenewu unachokera mumlengalenga, nunena Mawu awa, "Monga Yohane M'batizi anatumidwa kuti akatsogolere kudza koyamba kwa Khristu, utumiki wako udzatsogolera Kudza Kwachiwiri Kwa Khristu," pamene anthu zikwi zikwi anamva izi, ndipo a manyuzi anapereka umboni wake.

65 Ndikufuna nditi, ndipo ndikufuna aliyense amvetse za wosuma wakhungu uja amene akufuna kuchita kuona mwamuna amene ali ndi zipsyera za minga ndi misomali, ndi zina zonse zotero. Siziri choncho! Sikunaperekedwe lonjezo loterolo.

66 Timawerenga apa pa Luka, mutu 17 ndime 30 Yesu akulankhula kuti, "Monga kunali m'masiku a Sodomu, kudzateronso pamene Mwana wa Munthu adzaululidwa." Pamene akuululidwa! Ndikufuna mumvetse ichi kwa maminiti ochepa ngati mungapirire nane kwa timaminiti tingapo tokha.

67 Taonani, Yesu anali ndi maina atatu; Mwana wa munthu, Mwana wa Davide, Mwana wa Mulungu. Anali ndi maina atatu. Onse a munthu m'modzi yemweyo, koma

maina atatu. Chimodzimodzi monga Atate, Mwana, Mzimu Woyera, onsewo a Mulungu yemweyo, maudindo atatu.

68 Monga ine. Mkazi wanga amanditcha mwamuna wake. Ana anga alibe nazo zoti azinditcha ine ngati mwamuna wao, ine ndi ababa awo. Mzukulu wanga wang'ono amene wakhala apoyo, alibe nazo ntchito zoti azinditcha ine ababa, alibe nazo zonditcha amuna ake, iye ndi mzukulu wanga. Ndipo zonsezi ndi za munthu yemwe yemweyo.

69 Ndipo tikuona pamene Yesu anadza nayesa kudziulula Yekha ngati Mwana wa munthu (musaphonye apa), pamene Iye anadziulula, nadzitcha Yekha, nthawi zonse, "Mwana wa munthu," Israeli anachititsidwa khungu. Iwo sanadziwe kali konse zomwe mwana wa munthu ankatanthauza. Koma iwo ankati, "Mwana wa Davide," pamene Bartulomeyo Wakhungu anamthamangira namzindikira Iye. Davide ankatanthauza "Mfumu". Kumbukirani, Mwana wa munthu, Mwana wa Davide, Mwana wa Mulungu (amene ali Ambuye). Muyuda uyu analandira chimene anapempha chifukwa cha kuti anadzamulankhula Iye mu Dzina la Mwana wa Davide, Mfumu; Iye sanali Mpulumutsi koma anali Mfumu.

70 Koma pamene mzimayi wa Chihelene, wa Chisirofoninke anadza kwa Iye mu Dzina la Mwana wa Davide, Iye sanadzutse nkonse mutu Wake. Mkazi uyu analibe ufulu wakumulankhula Iye mu Dzina la Mwana wa Davide. Iye sanali Mwana wa Davide kwa mzimayi wa Chisirofonikeyo. Koma pamene mkaziyo anati, "Ambuye." Mwaona? Iye anali Ambuye! Osati Mwana wa Davide kwa mkaziyo.

71 Tsopano, chifukwa chiani Iye sanadziwidwe ngati Mwana wa munthu? Mwana wa munthu linali vumbulutso lauzimu, m'neneri. Mwana wa munthu amatanthauza "Mneneri."

72 Tsopano ngati mutatsegula nane mu Mabaibulo anu ku Ezekieli, mutu 2 pa ndime 1, mupeza Ezekieli anali mneneri, Mawu a Mulungu a tsiku limenelo. Ndipo Yehova Mwini anamutcha iye mwana wa munthu. Yehova anamutcha iye munthu, mwana wa munthu, chimodzimodzi

monga momwe Yesu anadziululira Yekha ngati Mwana wa munthu. Ndi chiani chimenecho? Mawu olonjezedwa a nthawi yawo akusandulika thupi, Mulungu yemweyo! Mulungu ndi Mzimu. Ndipo Iye anadziulula Yekha ngati Mwana wa munthu! Iye sanali pa nthawi imeneyo...

73 Iye anali Mwana wa munthu chifukwa anadza kudzadziulula Yekha kwa Israeli monga Mneneri, ndipo iwo anamukana Iye. Ndipo uwo unali uneneri umene anayenera kumulandira Iye, muDzina la Mwana wa munthu, Mneneri, chifukwa zinali zogwirizana ndi Mawu. Deutronomo 18:15, "Ambuye Mulungu wanu adzakudzutsirani mneneri monga ine." Ndipo pamene Iye anadza, Iye anadzizindikiritsa Yekha mu Utimiki Wake ngati munthu, osati Mwana wa Mulungu, Mwana wa munthu! Mulungu ndi Mzimu. Ndipo iye anadziulula Yekha monga Mwana wa munthu, chimene Iye ankadzitcha kuti ali. Ndipo iwo anachitidwa khungu ndipo sanakhoze kuchiona.

74 Koma tsopano kwa Amitundu Iye akudziulula Yekha, ndipo tsopano Mwana wa Mulungu amene ali Mzimu Woyera. Tsopano, Yesu anati, "Monga kunaliri m'masiku a Sodomu!"

75 Ndikufuna wosuma wakhunguyu kuti awone ichi. Iye ndi womasulira Mawu mwa Khungu nthawi zonse. Amatenga zilingaliro za mabungwe pa izi, ndipo sadziwanso zina zoposa pamenepo. Amatero pofuna kunyenga anthu, chifukwa iye ndi wonyenga pa chiyambi pomwe.

76 Yesu anati, "Monga kunaliri m'masiku a Sodomu, pamene Mwana wa munthu akuululidwa!" Mu masiku a Sodomu Mwana (amene anali Mulungu) anaululidwa mu thupi, amene anali kutchedwa nthawi ina Melkisedeki, Atate. Melkisedeki pa nthawi imeneyo analibe atate ngakhale amayi, ndipo analibe chiyambi cha masiku kapena kutha kwa moyo wake; chimene iye anali, Adakali yemweyo! Yesu ali ndi atate ndi amayi; koma Mwamuna uyu analibe ngakhale atate kapena amayi. Ndipo Iye anadzaonekera kwa Abrahamu mwa maonekedwe a Mwana wa munthu, Elohim, Yehovah. Mpingo tsopano watumikira nthawi yake kupyolera mu mbadwo wa mpingo, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera. Koma Yesu anati apa, kuti

Malaki 4 ndi Malembo ena onsewo akhale omveka kwa inu, onani, anati, "Mu masiku otsiriza, kutangoyandikira Kudza, kakhalidwe mu dziko lapansi kadzakhala ngati ka Sodomu, ndipo Mwana wa munthu adzadzilulula Yekha ngati Mwana wa munthu monga momwe Iye anachitira mu masiku a Sodomu."

77 Wosuma wakhungu, kodi ukuona zimenezo? Mawu Ake ndi owona. Osati zipsyera za misomali ndi minga.

78 Ndi Mwana wa Mulungu amene akudziwonetseranso Mpingo Wake, monga Mwana wa munthu!" Monga Mulungu Atate, Mulungu Mwana, Mulungu Mzimu Worera; ndi Mulungu yemweyo, makwaniritsidwe atatu mosiyana a Mulungu yemweyo. Tsopano, uyu ndi Mwana wa Davide... Mwana wa munthu amene akudzaululidwanso monga mneneri. Mwana wa Davide, Mfumu. Ndipo tsopano Mwana wa Mulungu mu mibadwo ya Mpingo, monga, pamene Mulungu si munthu, Mulungu ndi Mzimu, ndipo Mwana wa Mulungu ndi Mzimu woyera, umene ukuulula kwa anthu m'badwo wa mpingo. Koma apa palonjokedwa, "Mu masiku otsiriza, kuti Mwana wa munthu adzaululidwa!"

79 Wosuma wakhungu, kodi ukumva zimenezo? Ndipo ndikufuna kuti wosuma wakhungu'we udziwe kuti ife tikuziona, ife tikuzikhulupirira, Mawu amenewa akukwani-ritsidwa pamaso pathu ndipo tikudziwa kuti ali Choonadi.

80 Kwa Ayuda Iye anali Mwana wa Davide. Kwa Agriki Iye anali Ambuye, kwa ife Iye ndi Ambuye, kwa Amitundu. Ndiyeno m'masiku otsiriza, Iye ayenera kubwereranso monga Mwana wa Munthu, chifukwa Malaki anatilonjeza ife kuti kudzadza mneneri m'masiku otsiriza amene adzabwezera mitima ya anthu (kuwachotsa ku mabungwe) ndi kuwabwezera ku Mawu a pachiyambi, chikhulupiriro cha atate athu, pentekoste yoyamba. Ndipo pamene anatero, Yohane Woyera 14:12, ndipo zimene Iye anazichita ziyenera kuchitikanso. Chivumbulutso 10 analonjeza zinsinsi zonse. Muiziulula bwanji zinsinsizo? Kuona zimene Luther analephera, kuona zimene Wesley analephera, kuona zimene Apentekoste analephera, ndi kuulula zinsinsi za mu mtima, kuti zimveke kuti ndi Mulungu yemweyo mu mibadwo yonse, chimene sichiri china ayi koma Mawu a Mulungu akusandulikaso thupi

nakhalanso Mwana wa munthu. Sitikufuna kuti tiwone zipsyera za misomali; tikufuna tiwone Mawu akusandulika thupi. Taonani, Mulungu analonjeza zinthu izi tsopano, ndipo Iye akuchitanso monga momwe ananenera. Ndikananena zambiri, koma tidzangosiya phunziro lathu, nthawi yatha.

81 Bambo Osuma, ine ndikufuna inu kuti mudziwe kuti ine ndikhoza kuyitana mboni zikwi pano mazulo ano. Ine ndikufuna inu mudziwe kuti zinthu zimene Iye ananena kuti anazichita, ife ndi mboni kuti "Iye amasunga Mawu ake!" Pali misonkhano ya Mzimu Woyera yeniyeni! Pali mphamvu ya Mulungu yeniyeni! Ndipo pali lonjezo lenileni la kuti adzachira, pamene manja asanjikizidwa pa odwala. Ine ndikufuna inu mudziwe zimenezo. Ndikufuna inu mudziwe kuti Iye anati, "Monga kunaliri mu masiku a Sodomu, kudzakhalanso chimodzimodzi pakudza kwa Mwana wa munthu."

82 Ine ndine mlendo, ndipo ndikungochitira umboni wa chimene Baibulo limanena kuti ndi Choonadi, Ngati mutaona, Mngelo wa Ambuye amene anadza mwa maonekedwe a mwamuna, anali atalozetsa nsana wake ku hema, ndipo Iye anamuuza Abrahame zimene Sarah anali kuganiza. Yesu anati kuti zidzabwereza. Tsopano, ngati ndakuuzani Choonadi, tirole Mulungu atsimikizire kuti ndi Choonadi. Timulole kuti awululeno. Ndiye, sichikhala chinsinsi, tidziwano. Ine...ndikulisiyira bwalo lamulanduli mazulo ano lingaliro ili, kuti asankhe chochita. Tirole Mulungu amene anapanga lonjezo...osati za masiku a kale; iwo anatsimikiziridwa. Tirole Mulungu amene anapanga lonjezo kuti atitsimikizire lero, achite chimodzimodzi. Ena a inu mukuganiza mu mitima yanu, pempherani kwa Mulungu chifukwa cha matenda anu ndi kutunduzidwa kwanu, ndipo onani ngati Mulungu anaulula chinsinsi cha mu mtima. Ine ndikhoza kupikisana nanu nonse amene mungatero kuyambira mbali iyi mpaka kwinaku. Tsopano, kodi ndinganene motere ngati sindikuyima kwenikweni pa chimene Malembo amanena? Ine ndikufuna bwalo lino liwone kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero ndi nthawi zonse, kuti Iye amasunga malonjezo Ake. Ndipo Iye analonjeza kuti Yesu Khristu adzaululidwa mu masiku otsiriza, ngati Mwana wa munthu.

83 Mwamuna amene wakhala apayu akuvutika ndi nyamakazi. ine sindinakuoneni inu mu moyo wanga wonse. Ngati ziri zoon, kwezani dzanja lanu. Mukukhukupirira ine kuti ndikupereka umboni wooka wa Mawu a Mulungu? Awo ndi akazi anu amene akhala pafupi ndi inuwo. Iwonso akuvutika ali ndi chotupa pa mutu wao. Ndi zoon, kwezani dzanja lanu. Kodi mukukhukupirira kuti Mulungu akhoza kundiiza ine kuti inu ndi ndani? Ngati Iye ali Mawube, Mawu anadziwa zinsinsi za m'mitima. Inu ndi Bambo ndi Mayi Hunt. Ngati ziri zoon, kwezani dzanja lanu. Chifukwa chiyani simukukhukupirira?

84 Pano, pali bambo amene akhala apa, mutu wao atazyolika, akulira, akudzipempherera iwo wokha ndi akazi awonso. Aakaziwo sali pano. Iwo sali ndi inu mazulo ano. Iwo akuvutika. Kodi mukuganiza kuti Mulungu akhoza kundiiza vuto lawo, pamene iwo sali pano? Mukukhukupirira? Ndithu? Ine ndine mlendo kwa inu, sichoncho? Akazi anu ali ndi vuto la azimayi. Ngati ziri zoon, kwezani dzanja lanu, m'mwamba, kuti ife tirione. Ndipo dzina lanu ndinu a Smith. Kodi mukukhukupirira kuti Mulungu awachiza? Ngati ziri zoon, gwedezani dzanja lanu m'mwamba ndi kulitsitsa chonchi. Ndikukuuzitsani kuti mukhukupirire Yesu Khristu wabvumbulutsidwa mwa mwana wa munthu. Tsono kwa inu amene mumakhukupirira, iyi ndi mphamvu ya Mulungu amene adziwa ganizo liri lonse.

85 Pano pali mzimayi amene wakhala pano akundi-yangana, iye akubvutika ndi kuthamanga kwa magari. Mukukhukupirira kuti Mulungu akhoza kundiiza kuti ndinu ndani? Amakutchani inu Daisy. Ngati muli...kodi ndi zoon? Imikani dzanja lanu. Khukupirirani tsopano ndi mtima wanu wonse. Yesu Khristu akukonzani...akupatsani zofuna zanu. Mukuona, Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kunthawi zonse. Mukukhukupirira?

86 Pano pali Bambo wakhala kumbuyo akuyangana kwa ine, Iye ali ndi bvuto mumtima mwake. Chifukwa cha mwana wake, mwana wake ali ndi matenda a kuthamanga kwa magari. Mukukhukupirira? Awo ndi akazi amu amene ayamba kulira pafupi ndi inuwo, iwo ali ndi bvuto mumtima mwawo. Ndiro la a chemwali awo. Achemwali awo ali ndi bvuto la mtima, umawasautsa. Inu ndi Bambo

ndi Mayi Sickles. Ngati ziri zowona imikani dzanja lanu mmwamba ndi kulitsitsa chonchi. Ngati ndi mlendo kotheratu kwa inu, imirirani pa mapazi anu. Imirirani, ngati ndiri mlendo kwa inu mwa kuti sindikukudziwani.

87 Ndi chiani? Kukwaniritsa kwa Mawu a Mulungu mu masiku otsiriza! Wosuma, ndikufuna udziwe kuti Mawu a Mulungu ndi owona. Mulungu anandiuza ine zake 33 zapitazo. Ndakhala ndikuyembekezera nthawi yonseyi, koma zakwaniritsidwa pompano mazulo ano. Mulungu amasunga Mawu Ake! Iye ali yemweyo dzulo lero, ndi nthawi zonse. Mulungu akudalitseni inu; pitani mutalandira chimene mukuchikhumba tsopano.

88 Malingaliro anu ndiwo oweruza. Woweruza ayenera kulingalira chochita. Ndipo momwe muti muchitire kuyambira tsopano zifotokoza kapena ziwaonetsa anthu chimene inu mwagamula. Kodi Mulungu ndi wolakwa kapena Iye siwolakwa? Kodi mukukhulupirira kuti Iye siwolakwa, ndi kuti Iye amasungadi Mawu Ake? Ndi ife amene ali...Tikumvera za azibambo okalamba a Kusapirira, a Kusakhulupirira, ndi Kukaikitsa. Koma tsopano mukhulupira kuti Mulungu amasunga Mawu Ake? Malingaliro anu ndiwo woweruza. Ndipo momwe muti muzichitira kuyambira tsopano zidzatsimikizira kwa anthu kugamula komwe munali nako. Mukuona pamenepo? Tiyeni tiweramitse mituno.

89 Ine ndakuwuzani inu Choonadi mosabisa, Tikanakha- la ndi nthawi yongokhala pano, palibe Lembo mu Baibulo limene silipereka umboni wofanana ndi izi. Ine ndakhala wosabisa. Inu mukudziwa, nthawi zina, kuti ukhale munthu wosabisa si ntchito yophweka. Koma bola ngati Mulungu ayima pomwepo! Sizinali zophweka kwa Luther, Wesley, ngakhale mmodzi aliyense wa ena onsewo. Sizophweka kwa inu kapena aliyense amene mumayima chotero. Koma mazulo ano muyenera kudzisankhira kayimidwe kanu. Iye sanati...Iye anati, "Adzaika manja awo pa odwala ndipo adzachiritsidwa." Ngati inu mukhulupirira ndiye ine sindikusamala ngakhale zitachitika pomwe pano, ngati zitachitika sabata ya mawa, zitachitika zaka makumi awiri kuyambira lero; ngati inu mukhulupirira mwa ntheradi, ziyenera kuchitika. Ine...

90 Pali dotolo pano, monga momwe ndamvera. Ndikufuna kumuthokoza iye. Ndinali kwa wodwala ndinakawona wodwala, kanthawi kapitako, m'mawa wa lero ku chipatala amene watsala pang'ono kufa, momwe iwo akuganizira. Wangodyeka ndi kansara. Ndipo mzimayi wamng'onoyu anati kwa ine, "Adokotala anga aakulu akhala akudza kumisonkhano yanu, ndipo akuvomerezana nanu. Ndipo sizokhazo, koma, M'bale Branham, ndikufuna inu mudziwe, kuti iye akuvomerezana nanu kuti mundipempherere." Ngati ndikanasowa chithandizo cha mankhwala, ndikanafuna ameneyu akhale amene ati andipatse, mwamuna amene angakhulupirire Mulungu chotero! Inde. Amapezeka oterowo mu mayandedwe onse a moyo, mu maphunziro apamwamba onse.

Tiyeni tikumbukire, kugamula ndi kwanu tsopano.

91 Ambuye Yesu, ndayesetsa kufotokoza Mawu. Inu mwachitira umboni kuti ndi Choonadi. Mboni zanu, tikanakhoza kuziyitana mazana, komabe tangokhala kuti tiribe nthawi. Panonso pali mipango, kuti aliyense amene akagwire iyo akachiritsidwe. Ndikupereka pemphero langa, ndi chikhulupiro, palimodzi ndi gulu lina la okhulupirirali, chifukwa cha awa amene alephera kukhala nafe pano. Atasangalala ndi kupambana kwa Mulungu. Akhoza kukhala akudwala mwa kuti sakanatha kudza. Azigogo okalamba amene akuvutika kumbuyoko mu chipinda, atasamira pa kandodo koyera, mazulo ano, akuyembekezera kulandira mpangowu. Lolani mphamvu ya Mulungu wa Mphamvuzonse kuti ipite nawo, iwadzoze iwo ndi kudzoza komweko kumene kunali pakati pa msonkhanowu madzulo ano. Ndipo achire Ambuye. Tikupereka pemphero ili m'malo mwawo, chifukwa iwo panalibe pakati pathu. Koma Inu ndi opezeka pali ponse. Mukhale muli kumeneko mukutsimikizira Mawu Anu, kupyolera mu Dzina la Yesu Khristu.

92 Tsopano lolani Mzimu Woyera ndithu, osati zongotengeka, osangoti kachiyembekezera ka m'deram'dera, koma kugamula kwenikwene kuperekedwe pa izi, ndi amene ndikuwatcha, "khothi madzulo ano." Aliyense wa iwo atapereka umboni wofanana, pamene akutenga makadi a anthu oti apemphereredwe nawanyamula m'manja awo, pamene akudutsa pa guwali.

Mutalola pamene iwo ali...pamene alalikiridwa mogwirizana ndi pa mutu 16 wa Marko Woyera, "Adzayika manja awo pa odwawa ndipo adzachira." Monga momwe wantchito Wanu wosankhulidwa ndaima apa, ndi pamene ife tikuyika manja athu pa iwo, Ambuye, zonse zithe kwathunthu. Atuluke muno atangosangalala, nayiwala mavuto amene anali nawo, chifukwa iwo akutsimikiza kuti, monga Abrahamu analiri, pakuti Mulungu akhoza kukwaniritsa malonjezo amene anapanga. Tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen.

Ndimkonda lye, Ndimkonda lye,
Anandikonda koyamba
Nandigulira Chipulumutso
Pa mtanda pa kalvare

93 Ndi angati amene ali ndi kugamula? Kwezani dzanja lanu, "Ndiri ndi kugamula kwanga nane." Chabwino, bwalo, inu mudzatumikiridwa mogwirizana ndi Mawu Oyera a Mulungu. "Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira." Ine sindikusiyani inu kuti mukhale apa, mukaganiza kuti iyi ndi mphatso yongofuna kumuchititsa wina kukhala woposa anzake. Inu muli ndi azibusa a umulungu apa. Iwo ali pompano, tingowafunsa iwo kuti ayime ndi ine pa guwa lino. Iwo asanjika manja awo pa anthu omwe nditi ndiwasanjika manja. Iwo ndi amene anatiyitana ife kuno, ndipo iwo ndi anu...monga mboni za Mulungu. Iwo akuchitira umboni Choonadi. Tsopano, simungati, "M'bale Branham anandisanjika manja," pakuti manja sasiyana ndi manja a ena onsewa. Ndi chikhulupiriro chanu, kugamula kwanu kumene muli nako pa Mawu a Mulungu. Mulungu amasunga! Ngati Mulungu angasunge gawo ilo la Mawu natsimikizira kwa inu, pamenepo ndiye kuti ndinu ochiritsidwa kale, chifukwa ndi mikwingwirima Yake inu munachiritsidwa.

94 Tsopano, ndikufuna onse amene ali mbali iyi kuno, amene ali ndi makadi kuti apemphereredwe, imirirani mbali iyo cha ku khoma. Tsopano, onse amene ali mbali iyi, amene muli ndi makadi oti mupemphereredwe, imirirani pakatipa mwa mzere choyang'ana mbali iyo. Ndipo onse amene ali mbali iyi, amene ali ndi makhadi oti apemphereredwe...Tsopano, apa-mbali iyi kuno, amene muli ndi makhadi, mudze mbali iyi choyang'ana mbali iyo,

ndipo ndi pamene tidzayamba kupempherera anthu a pamzere. Onse amene muli mkhonde ndi makhadi oti apemphereredwe, idzani kuno ndi kutsatira pambuyo pa gulu linalo pamene akudza. Pamene iwo akudza, ine...

95 (M'bale Branham alankhula ndi atumiki pa guwa - Mkonzi.) Inu mukufuna kuti ndiitane atumiki ena? Kodi kuli bwino kuti tikhale ndi mboni? Chabwino, zavomerezeka ndi inu nonse? Kugamula kwanu nkotani pa mulanduwu? (M'bale Branham ayankha, "Ndikudziwa kuti zinthu zimenezo ndi Choonadi." - Mkonzi.) Chabwino.

96 Abusa akufuna kudziwa, akufuna chiyanjano ndi atumiki ena. Akufuna mtumiki aliyense muno amene amakhulupirira Mulungu, nakhulupiriranso za kusanjika manja pa odwala, ngati kugamula kwao mazulo ano, kuli koti ndi "Choonadi," awa akukuitanani monga anzawo kuti mubwere pano ndi kudzaima nafe pa guwa pamene tikupemphera. Azibusa onse amene ali ozadzidwa ndi Mzimu wa Mulungu, amene kugamula kwanu tsopano ndiko kuti mukukhulupirira kuti Iye ndi yemweyo dzulo, lero ndinthawizonse, amene mukukhulupirira kuti Marko 16 ndi Choonadi, azibusa awa akufuna kukuitanirani kuno tsopano monga anzawo mu Uthenga. Bwerani kuno ndi kuyima pa guwa nafe pamene titi tipange nzere wa anthu oti apemphereredwe, kuti tipemphere. Pomwe pano, aloleni adze kuno. Azibusa onse mu nyumba ino, ziribe kanthu kuti ndinu a dinomineshoni yanji. Iwowa angondipempha ine kuti ndikufunsemi. Idzani pano ngati mukufuna kudza tsopano, ndipo pangani nzere kuti mupemphereredwe, inu mudzipempherera odwala, inu mudzipempherera odwala, pakusanjika manja anu pa odwala.

97 Ndiangati muno amene alibe...amene ali bwino, tsopano, ndipo simukusowa kupemphereredwa koma ndinu okhulupirira, kwezani manja anu. Kodi mungandilonjezenso kuti mudzipemphera palimodzi ndi azibusawa pamene ife tikupempherera anthu awa? Bwanji ngati awo amene ayima apowo akanakhala amayi anu? Bwanji akanakhala akazi anu? Bwanji akanakhala abale ndi alongo anu? Kumbukirani, iwo ndi amayi a wina, ndi achimwene a wina, ndi chemwali a wina, ndi m'nyamata kapena msungwana wa amayi ena, ndi a uje kwa wina. Ndipo ife

tichita kwa ena monga momwe ena akanachitira kwa ife. Tsopano, ndikufuna inu, aliyense akhale modzichepetsa kwa Mulungu napemphera.

98 Ndipo pamene tapanga mizereyi tsopano, tasiya mpata woti azidutsamo, ine ndikufuna atumiki tsopano kuti adze napange mizere iwiri mbali ziwiri za pa guwali, kochokera uko kufika uku, apange mizere iwiri kuti anthu azidutsa pakati. Ndiika cholankhulirapochi kumbuyuku, Bambo a Borders akhala atayima apa akutsogolera nyimbo. Ndi momwemo, mizere iwiri kuchokera uko kunka uku, kuti anthu...

99 Tsopano, kwa aliyense wa inu amene mwayima pa mzere, mupange mizere iwiri kuti Satana wosuma, adziwe kuti inu mwatsimikiza mtima. Pongokhala kuti mwakhulupirira kuti zimene mukufuna ndi Mawu a Mulungu, ndipo ndi Choonadi, ndipo inu mukudza pa nzere kuti tisanjike manja pa inu. Ndipo wonama awoneka. Zochita zanu zisonyeza kuti kugamula kwanu kunali kotani. Kwezani manja anu ndikuti, "Ine ndikulonjeza Mulungu zimenezo." Onse amene ali pa nzere.

100 Tsopano tiyeni tipemphere. Atate anthu a kumwamba,...anthu awa, madzulo ano, anatengedwa ngati khoti. Ine Ambuye, ndikuona kuti munali ndi...mulandu weni weni. Pilato sanakupatseni chiweruzo choyenera, iye anatenga mboni zabodza. Koma inu munazitsutsa izo. A - Mboni Yotchinjiriza, Mzimu Woyera bwerani mudzatsimikizire Mawu pamaso pa anthuwa. Inu munali pa mulandu wosakondera. Ndipo anthu alingalira bwino, agamula okha lero, ndipo akudza kudzalitsimikizira dziko lapansi kuti iwo akukhulupirira kuti Mawu Anu ndi otero. Iwo akhala ali mu matchalitchi kuno, ena a iwo namati, "Ndiwone mukuchita ichi, ndione mukuchita icho." Choncho si momwe Mawu Anu anenera. Mawu amati, "Iwo adzachira." Ndipo ife tadza ndi mboni zina paguwa pano, kuti zitsimikizire kuti zimenezo ndizo zomwe munanena. Inu mumachita zinthu mwa njira Yanu.

101 Tsopano, ndikupemphera, Atate, kuti mupereke madalitso madzulo ano kwa anthu awa. Monga Wantchito Wanu, pamodzi ndi antchito anu mazana a iwo pano, tikupereka mapemphero athu chifukwa cha anthu awa.

Dzozani azibusa abwinowa, Ambuye. Okayikira ngati atadzadutsa apa, kapena osakhulupirira, kapena Bambo Kusapirira, kapena aliyense mwa iwo otsutsa, otonza amene akhala alipo mu mibadwo yonse, ngati ati adutse pakati pa anthu awa, bwalo ili madzulo ano litatsutsa pamodzi, umboni wao. Kuti, ngakhale anene kuti chiyani, monga momwe kunaliri m'masiku a Sodumu, zipite ku chionongoke. Momwe iwo ankatonzera namaseka! Koma zinalibe ntchito, okhulupirira anangopitirira ndi Mawu. Ndipo ife takonzeka kukangamira pa Mawu Anu madzulo ano, Atate. Tsopano, monga Mawu Anu anatero, palimodzi ndi azibusa Anu pano tikufuna kusanjika manja pa anthu awa, mutalola mphamvu za Mulungu Wamphamvuzonse, amene ife tikudziwa kuti ali pano kudzatsimikizira Mawu, pochiza aliyense wa awa. Mu Dzina la Yesu Khristu Ambuye wathu. Amen.

102 M'bale Roy, idzani cha kuguwa kuno. Mutu uliwonse uwerame tsopano, aliyense azipemphera ndi kuyimba. Ngati simukupemphera, ziyimbani Only Believe. Pamene mukudutsa, muzikhulupirira kuti Ali pano. Ziribe kanthu zimene muti muzinena kapena kuchita, izo ziri kwa inu. Ngati mukufuna kufuula, fuulani. Ngati mukufuna kuyenda...Ngakhale mutafuna kutani, ingokhulupirirani Mulungu. Nyamukani nimuyende ndi kuti, "Pakwanira mu mtima mwanga." Monga momwe mukanachitira popita ku dziwe kukabatizidwa. Zakwanira, ngati mukukhulupirira. Inu ndi Akhristu ngati mukukhulupirira. Si choncho? Ndipono muchiritsidwa ngati mukukhulupirira. tiyeni tipemphere tsopano Chabwino, M'bale Borders (M'bale Branham apempherera odwala. Malo opanda kanthu pa tepi - Mkonzi) Ingokhulupirirani!

Mpaka pomwe tidzakomana
Pa mapazi a Yesu,
Mpaka pomwe tidzakomana
Mulungu akuyanganireni.

103 Ine ndalalikira Mawu a Mulungu kwa inu. Mu Dzina la Yesu Khristu, aliyense wa inu alandire chimene wafunsa. "Ngati munena kwa phiri ili 'Suntha' ndipo osakayikira mu mtima wanu, koma kukhulupirira kuti chimene mwanena chichitika, mukhoza kukhala nacho chomwe mwanena." Mukapemphera, khulupirirani kuti

mulandira chimene mwafunsa, ndipo chipatsidwa kwa inu. Ine ndikulalikira mu Dzina la Yesu Khristu. Ndikukhulupirira kuti kugamula kwathu kwachitika ndipo kwatha ndi momwe tachitira zikusonyeza tsopano chimene tikukhulupirira, ndi kudziwa kuti Iye amachiritsa. Ngati sindidzakuonaninso tsidya lino la mtsinje, ndidzakumana nanu tsidya linalo. Ndiye Mzimu Woyera Amene anali Mlendo wathu sabata lino, Kuno pamene Anali kutumikira kwa ife, Iye akhale mboni kwa Inuyo kuti tanena "Choonadi." Mpakana nthawi imeneyo.

Mpaka pomwe tidzakomana!
Mulungu akuyanganireni!

104 Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano. Mwa kachetechete zedi, mokoma, (M'bale Branham ayamba kung'ung'uza Mpaka pomwe tidzakomana-Mkonzi) Tsiku limenelo titadzayima pamaso Panu, mwa Ulemelero Wanu, titadzakhala tonse Ambuye pamene tamulandira Iye. Mulungu akhale nanu. Ndikukuthokozani inu nonse.

Mulandu

(*The Trial*, Vol. 12 No. 2)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingezezi Lamulungu Madzulo, pa 19 Epulo, 1964, mu Tampa, Florida, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingezezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa chaka cha 1987 ndi Voice of God Recordings.

VOICE OF GOD RECORDINGS

P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana, U.S.A. 47131

Copyright notice

All rights reserved. This book may be printed on a home printer for personal use or to be given out, free of charge, as a tool to spread the Gospel of Jesus Christ. This book cannot be sold, reproduced on a large scale, posted on any website other than www.branham.org, stored in a retrieval system, translated into other languages, or used for soliciting funds without the express written permission of Voice Of God Recordings®.

For more information or for other available material, please contact:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org